



Noah's Ark reloaded (Before the great rain)

Notes:

This text has been written for four narrators. The texts, however, can be read by more or fewer persons. More important is a feeling for the rhythm. A change of voices at different points could be effective.

Moreover, there should be another person in the background speaking the Bible quotations etc.

*Words which should be emphasized are written in **bold**. Pauses are marked by indents (-----). The words written in red should be practised before, as their pronunciation is not always easy.*

Between the chapters there will always be music and pictures, the only exception being the transition from chapter 2 to chapter 3. At this point there will be just a short pause, but this has been marked separately.

At the end of each page there is a short note which narrator will continue. This is meant to help preparation and should not be read.

In the [square brackets] are notes for the technician. If there is written „Klick“, the technician must manually forward a picture. These happens mostly during the reading and at the transition to music between the chapters. During the music, the pictures change automatically and also to the next statue of the new chapter.

Mawu ochokera kumbuyo:

Tsiku limenelo madzi anaphulika kuchokera mu nthaka komanso kumwamba kwa dziko lapansi. Mvula inagwa kwa masiku makumi anayi masana ndi usiku omwe. Chilichonse cha moyo chimene chimayenda pa dzikoli chinafa, mbalame, ziweto, ngakhaleenso nyama za ku tchire. Indetu chilichonse cha moyo cha padziko lapansi chinafa kuphatikiza ndi anthu omwe. Nowa yekha ndi zose zomwe analowa nazo mu chombo ndi zomwe zinapulumuka.

GAWO 1 [Picture 1]

- A: Izi ndi zomwe **Baibulo** limanena.
- B: Zimenezi zimapezekanso mu buku lopatulika la chisilamu lotchedwa **Korani** komanso la chiyuda lochedwa **Tora**.
- C: Nkhani zangati za chigumula cha Nowa zimapezekanso mu **nthano** za chikhalidwe komanso chikhalidwe za mbiri ya anthu osiyanasiyana.
- D: Mtheradi. Nkhani za chinonongeko cha dziko lapansi zilipo.
- C: Eyetu. Nkhanizi zilipo mu mbiri ya anthu a ku **Ulaya** komanso anthu otchedwa ma **Borijinzi**, ngakhaleenso ku ma tchaina.
- A: Sikawirikawiritu kuti chionengeko chimangobwera pa dziko lapansi popanda chopangitsa. Nthawi zambiri chimabweretsa ngozi ngati izi pa dziko ndi uchimo. Mulungu amakhala akulanga anthu chifukwa cha machimo.
- B: Eyetu machimo amapangitsa kuti Mulungu alange anthu ake ndi ngozi ngati izi.
- D: Mwa njira ina tinganene kuti anthu asamade wina aliyense koma iwo okha eni ake ngozi za dzidzidzi zikamachitika pa dziko lapansi pano.

[Klick to Picture 2]

Next: B

GAWO 2 [Picture 4 and Picture 5, change automatically from Picture 3!!!!]

- B: Lerotu ndi pa ... mwezi wa novemba. Mpaka lero mvula siinabweretu. Ndiyetu mukamakamba za mvula yobweretsa madzi osefukira, sinkhamba kamwa chabe kodi ?
- A: Zikuoneka ngati chonchoditu.
- C: Indedi. Nkhani zongopeka izi.
- B: Maloto chabe awa.
- A: Ngakhale mukutero. Dziwani kuti izi zikuchitikadi mu njira zosiyanasianatu.
- C: Nthawi zina mofulumirapo
- D: Nthawi zina mochedwerapo
- C: Nthawi zinatu chionengeko cha dziko lapansi sichimaoneka ndi maso. Dziwani izi.
- D: Ndi mvula **[Klick to Picture 5]**
- C: Komanso olo popanda mvula
- A: Komansotu olo popanda chombo
- C: Olo popanda Nowa
- B: Koma ndi ife.
- D: Eyetu ndi anthufe pamodzi ndi zinyama za dziko lapansi pano.

Attention: no pictures and no music

GAWO 3 [Picture 6 and Picture 7, change automatically from Picture 5!!!!]

- D: Izi zikuthauza kuti.
- C: Kusintha kwa nyengo kukukhudza tonse.
- D: Kuthauza kuti...
- B: Ndi kusintha kwa nyengo palibe opambana koma tikapanda kusamala tonse tivulala.
- C: Kuthauza kuti. **Next: A**

- A: Madzitu akachuluka mu Nyanja za mchere chifukwa cha kusintha kwa nyengo tonse timira ndinthu.
- D: Za bodzatu izi.
- B: Ku gombe la Nyanja ya Miami ku Amerika, mitengo ya nyumba ikutsika chifukwa cha kuchuluka kwa madzi. Nyumba zikumira. Misewu kudzadza ndi madzi sizinthunso za chilendo ayi. Anthu amene amakhala kumeneko ali pa mavuto aakulu. Komanso iwo ali ndi mayankho amavutowa. Kungoyenera kusamukira ku mtunda kutali ndi Nyanja.
- C: Mufuna kundiuza kuti mitengo ya nyumba mu malo omwe anali onyozeka yayamba kukwera? Omwe amakhala malo onyozekawa ayamba kusamuka chifukwa mitengo yakwera kwambiri. Sangakwanitsenso kulipira. Nawonso ali ndi vuto. Komatu, kapena nawonso angakhale ndi mayankho a mavuto awowa? Chifukwatu alibenso kuthekera kokhalabe ku gombe la Nyanja ya Miami. Anthu osauka omwe amapanga lendi ndi amene akuvutika pamene eni nyumba akulemera ndi kukwera kwa mitengo yopangira lendi.
- D: Nkhani ngati izi si ku Amerika kokhatu ayi. Zikuchikitanso ku mayiko ena.
- A: Omwe ali ndi chuma, ndalama, amatha kudzithandiza wokha ku ngozi zogwa mwadzidzidzi.
- C: Komansotu amatha kudziteteza nthawi zina popondereza anthu osauka.
- D: Nthawi zina amagwiritsa ntchito zida za nkondo kumene podziteza
- A: Amene ali ndi chuma **[Klick to Picture 7]**
- B: Ali ndi mipanda
- C: A kumpanda
- D: Ali ndi zida
- A: Amapanga ndalamatu kukagwa ngozi zadzidzidzi.
- C: Anthu omwe alibe chuma siamene amapangitsa kuti chilengedwe chionongeke nkubweretsa ngozi zadzidzidzi.
- A: Anthu omwe sanakhalepo ndi galimoto. Sanakwerepo ndege.
- D: Ndi omwe amavutika kwambiri.
- D: Omwe ali osaukatu ndi omwe mau awo saamveka komanso ndi omwe amavutika kwambiri ngozi za chilengedwe zikagwa. **Next: A**



- A: Ndimadabwa kuti inu anthu olemera, mumamva bwanji mukamaona izi zikuchitika?
- D: Munayamba mwakhala pansi nkuganizira kuti anthu osauka aja omwe kulira kwawo sitikumva, kuti mawu awo ngotani?
- B: Kodi nkulira kwawo amati chani anthu amenewa?
- C: Kodi malangizo amene angatipatse ndi oti chani, anthu amenewa?
- D: Kodi sangatiloze chala kuti ndi ife amene tikuonononga chilengedwe?

[Klick to Picture 8]

GAWO 4 [Picture 14, 15, 16, 17, 18, 19, change automatically from Picture 13!!!]

- B: Ndimakhala kudera kozizira kwambiri kotchedwa **Arctic**. Ndine ice bear, imodzi mwa nyama za mtchire zomwe zikuvutika chifukwa cha kusintha kwa nyengo. Koma enanu, sizikukukhudzani ayi olo mpang'ono pomwe. [Klick to Picture 15]
- C: Ma ice bear alipo mdziko lapansi pano pakati pa 20 000 ndi 25 000. Komatu chiwerengelo chake chikuchepa kwambiri.
- B: Mwa njira yina ndinene kuti ife ma ice bear tikutha chifukwa madzi ouma omwe ndi malo omwe timakhalamo akusungunuka tikuona ndi maso athu. Malo omwe timapeza chakudya chatu aonongeka ndi kusintha kwa nyengo.
- C: Mphepo ya nkuntho ikukankhira chakudya ku nyanja ya mchere.
- B: Ifetu timadziwa kusambira. Koma abale ngakhale odziwa kusambirayo amatopa makamaka ngati ulendo watalika.
- C: Ngati pamene zafikapa. [Klick to Picture 16]
- B: Zafikapotu [Klick to Picture 17]
- C: Chakudya chatu, nsomba, zacheperatu. [Klick to Picture 18]

Next: B

- B: Kuonjezera apa, mafuta aononga madzi athu mu nyanja. Kungobwelera mbuyo pang'ono pa nkhani ya kusungunuka kwa ice ku Arctic, kumbukirani kuti izi zikachikita ife timafa. Zikaterere dziwani kuti nanunso muli ndi vuto. Mwina simungalione lero koma dziwani kuti vuto lilipo ndipo likupezani posachedwapa. **[Klick to Picture 19]**
- C: Si ice yekha amene akupangitsa nyanja kusefukira. Nyanja sisintha kwambiri koma ice amafufuma mwansanga kusiyana ndi madzi.
- D: Komansotu pali madzi ena amene ali pa dzikoli.
- C: Chilumba cha Greenland chonse chimakutilidwa ndi ice yekhayekha.. koma pamene ndikulankhula pano madzi onse akusungunuka mwansanga koposa kale.
- A: Pofika mwezi wa June chaka chino, chilumba cha Greenland madzi ake omwe anasungunuka ndi okwana ma billion awiri pa tsiku.
- C: Dziwani kuti ice pachilumbachi atangosungunuka madzi mu Nyanja zikululuzukulu angachuluke ndi 7.4 m.
- D: Mukafika ku **Antarctic**, kumwera kwa dziko lapansi nakonso kumayenera kukhala ice yekhayekha.
- C: Komatu nakonso kuli zomvetsa chisono. Ice akusungunuka momvetsa chisoni kwambiri.
- B: Madziwa akusungunuka mkumakafika ku nyanja zazikulu. Ndithu tonse timira.
- C: Izi tiyeni tivomere kuti sizichitika lero. Koma mukudziwa kuti madzi mu nyanja za mchere atongokwera ndi 1 m, dera lalikulu la ku Ulaya kumpoto kwa Holland ndi Germany kudzakhala mmadzi.
- D: Ku Bangladesh nako, ku Asia, gawo lalikulu lidzadzadza ndi madzi. Anthu mazanamazana adzasowa pogona.
- C: Mukhoza kumanga zipupa/makoma otchinga madzi a ku nyanja kuti asafike pa nthaka koma dziwani kuti izi ndi zofunika ndalama zambiri zedi.
- D: Bangladesh ndi dziko losauka kwambiri.
- A: Komanso vuto lina ndi lokuti madzi a anthu a ku Bangladesh amachokera ku ice wa ku Himalaya.
- Next: D**

- D: Anthu ambiri kumeneko amamwa madzi ochokera ku Himalaya. Kusungunuka kwa ice ku phirili ndi ngozi yayikulu.
- B: Basi, zaticwana izi.
- C: Tonse timadziwa kuti ice amathandiza kuti mphamvu za dzuwa zichepeko pa dziko lapansili.
- B: Mjintchi wa ice ukachepa, dzuwa limatenthetsa madzi mwansanga. Izi zimapangitsa kuti ice azisungunukanso mwansanga.
- A: Chaka ndi chaka ice amasungunuka ku North ndi South pole. Mtsogolo muno mwina cha mma 2030 ice adzatheratu mu nthawi yotentha. Nyanja zikuluzikulu madzi ake adzaonjezekera.
- D: Ku Alaska ndi ku Siberia nakonso ice akusungunuka chimodzimodzi. CO2 ndi Methane amene anali mu ice akulowa mu mpweya wa dziko lapansi pano.
- C: Chifukwa cha izi, kutentha kukuonjeza.
- B: Ndiye kupusa kwa munthu ndi kwakuti, mmalo mopanga chombo, akupanga ma bwato omwe akutenga anthu kupita nawo kukaona kusungunuka kwa ice ku Nyanja za Arctic ndi Antiarctic.
- C: Mabwato omwe amatulutsa mpweya wambiri wa CO2 kuponsanso ndege.
- B: Ili sivuto lathu chifukwa mwinanso tsopano mtundu wa anthu onse utha psiti!

[Klick to Picture 20]

GAWO 5 [Picture 28 and Picture 29, change automatically from Picture 27!!!]

- D: Ineyo, mwandiona. Ndimakhala ku dera labwino la ku Ulaya. Dzina langa ndine njuchi. Ndine onenepa. Mmene mukundioneramu. Anthu amaona ngati sindikwanitsa kuwuluka chifukwa chonenepa. Koma taonani. Ndikhozatu kuwuluka.
- A: Malo anga akuchepa chifukwa cha kusintha kwa nyengo. Kumwera kwa dziko lapansi, ku afirika kukutentha koopsya pamene ku Ulaya kukuzizira koopsya. Izi zikapitilira inetu basi ndisowa pa dziko lapansi pano. Zikangotero, mukhala ndi vuto lalikulu kwabasi.

Next: D



- D: Ine njuchi ndimakupatsani inu anthu chakudya, uchi. Komanso ngati sindipanga pollinate zakumunda kwanu ndiye kuti zakudya kwanu zisowa pa dziko lonse. **[Klick to Picture 29]**
- A: Chabwino. Zoulukauluka zinzanthunso zikuchepa. Anthu mukhala ndi vuto lalikulu.
- D: Akuluaukulu, kodi njuchi ndi zoulukazi zikachepa kapena kutheratu padziko pano, amene adzipanga polinate mbeu zanu ndani ?
- A: Baibulo limatiuza kuti kalekale anthu anamuseka Nowa mmene amakonza chombo chake. Koma mvula itayamba, poyamba anthu anatenga ma umbrella awo. Iwotu anaganiza kuti izi zithandiza poti monga mwa nthawi zonse mvula ikagwa, imasiya. Koma inu, sinthawi zonse zimaterotu. Mvula ikugwabe anthuwo amati, ahhh zikavutitsitsa tiona chochita, mwina tisamukira ku mtunda, ku phiri.
- C: Komano nthawi ya Nowa madzi amagwa kuchokera ku mwamba ngati mvula ena akutuluka ngati kasupe. Kunalitu madzi oti sanaonekenso padziko lapansi pano.
- B: Ehhhh! Abale nthawi imeneyo madzi amatuluka ming'alu, mmiyala, hhhhh inu pena paliponse panali madzi okhaokha. Anthu anasowa chochita.
- C: Nanga lero?
- D: Masiku ano kuli technology. Nzosavuta izi kuthana nazo zitakhala kuti chigumula ngati cha Nowa chabweranso. Munthu ndi wanzerutu.
- A: Ukutu ndiye kuganiza kopepera. Technology imakhala ndi malire.
- D: Paja ndi chizolowezi chanu chokonda kuyang'ana kumbali pakakhala mavuto eti. Pokhapo anthu ndinu akatswiritu.

[Klick to Picture 30]

GAWO 6 [Picture 35 and Picture 36, change automatically from Picture 34!!!]

- C: Tandiyang'anani. Ndimakhala kutali ku Asia patizilumba totchedwa Borneo ndi Sumatra. Ndine Orang-Otun. Kwa ine sizodabwitsa kuti anthu akudula mitengo mu nkhalango imene ife timakhala. Koma akuluakulu masiku ano zafika posauzana kuona ndi mmene anthu akudulira mitengo.

[Klick to Picture 36]

Next: B

- B: Tinene kuti njira imodzi imene anthu tikuonengera chilengedwe ndi kugwiritsa ntchito magalimoto komanso ndege. Izi zimaotcha mafuta kuti zigwire ntchito. Potero zimatulutsa mpweya oyipa wa CO₂. Anthu izi timadziwa koma sitikufuna kuchepetsa kapena kusiya kumene kukwera magalimoto ndi ndege.
- C: Masiku ano tikuti tikupanga magalimoto omwe akutulutsa mpweya ochepa wa CO₂.
- A: Njira yabwino yopewera kunononga chilengedwe nkupanga mafuta a magalimoto ndi ndege ochokera ku zomera.
- C: Ngati palm oil. Kupanga izi kungakhaletu chisankho chabwino zedi.
- B: Mumadziwa kuti ifeyo anthu ndi zomera timadalirana? Zomera zimatipatsa O₂ umene ifeyo ndi nyama zina timapuma. Ife timapuma CO₂ umene zomera zimagwiritsa ntchito popanga chakudya chawo. Zomeratu zimachotsa mpweya oyipa wa CO₂ pa dziko.
- A: Vuto ndi limodzi. Mmene dziko lapansi Mulungu analikonzera malire ake ndi omwewa. Ife sitingathe kulikulitsa dzikoli mpang'ono pomwe.
- D: Ndiye tisinthe kuti malo mmene timalima chimanga tidzalemo mbewu zopangira mafuta monga palm oil kuti tisiye kuononga chilengedwe kodi ?
- C: Mwaononga kale nkhalango zikuluzikulu monga ku Sumatra kwathu kunali nkhalango yowilira. Pano ili kuti ?
- B: Nkhalango zomwe zimatulutsa mpweya wabwino wa O₂.
- A: Izitu ndi nkhalango zomwe zimasunga CO₂ komanso mpweya wina oyipa. Pano mpweya oyipa onse ukubwelera padziko chifukwa mitengo kulibe.
- B: Kudula mitengo pofuna kuteteza chilengedwe?
- D: Amene akupindula ndi izi akutiiza kuti iyi ndi njira yabwino yothanirana ndi kusamala kwa chilengedwe.
- B: Pano anthu mukupanga mukuti magalimoto oyendera magetsi.

Next: A

- A: Mukapanga ochepa mmene zilili pano zikhoza kukhala ndithu zinthu za nzeru. Koma tangoganizani kuti magalimoto onse alipo panowa omwe amayendera petulo titawasandutsa oyendera mphamvu ya magetsi sipadzakhalatu magetso okwanira pa dziko lapansi. Tiyeninso tiganizire zida zopangira ma batile a galimotozi. Nkuonononga chilengedwe kokhakokhatu uku.
- C: Nchifukwa chake ife tikudandaula kuti malo athu atheratu ndithu. Pano kulibenso nkhalango imene kale inali mudzi wathu.
- B: Masiku ano mvula ikugwa moonjeza. Ndiyenso kukafuna kutentha inunso mukudziwa mmene kukumaotchera. Nchifukwa chake madzi okokolola nyumba ndi nthaka, moto olusa ndi chilala sizachilendonso masiku ano pa dziko lapansi. Miyoyo yahtu ili pa chiopsezo ndithu.
- C: Mwinatu kungofa ndi bwino kusiyana ndi kumanzuzika ndi kutentha pa dziko lapansi pano.

[Klick to Picture 37]

GAWO 7 [Picture 44 and Picture 45, change automatically from Picture 43!!!]

- A: Ineyo ineyo. Mwandiona. Ndimakhala ku Eurasia. Munyengo zabwino ndimapezeka kuyambira ku Ulaya mpaka ku Japan. Ndine mbalame yotchedwa Cuckoo. Anthu amanditchukitsa kuti ndine waulesi mkubereka. Komatu izi sizoono ayi.

[Klick to Picture 45]

- D: **Choka iwe. Ndiwatsoka chabe.**

- A: Tandifunsani kuti Cuckoo Cuckoo, tandifunsani kuti ndikhale moyo nthawi yaitali bwanji pansu pano, nditani? Kalekale anthu amawerenga kuti ndilira kangati, kamodzi kokha basi ndiye kuti

- D: **Matsoka, minyama.**

- A: Ndiyeno ndikufuna ndikufunseni kuti kodi ndikhala moyo zaka zingati? Ndipo chifukwa chimene mukuganizira choncho ndi chani?

Next: B

- B: Chifukwa cha kusintha kwa nyengo, pothawa kuzizira kwa ku Ulaya mbalame zina zikumapita kumwera kwa dziko lapansi mochedwa. Pobweleranso ku Ulaya pothawa kuthentha kwa ku afrika zikumabwerako mochedwa.
- A: Kusintha kwa nyengo kwandikhudza zedi. Ndikabwelera ku Germany mu April ndimappeza kuti mbalame zinzanga zaswa kale mazira awo. Sindingathe kuiikira mazira mu chisa chawo. Eyetu. Nthawi nthawi zina ndi ineyo amene ndimakhala ndi
- D: **Matsoka.**
- A: komatu siine ndekha watsoka ngakhale mukutero. Mbalame zinanso zilipo za tsoka. Monga fly catcher. Mbalame imeneyi imabwera ku Ulaya nthawi ya dzinja chifukwa choti zouluka zimakhala zitachuluka. Komano masiku ano zoulukazi zikumabwera msanga izo zisanafike. Choncho sizikumapeza chakudya.
- D: **Matsoka okhaokha awa**
- A: Komatu ndati sindife tokhatu.
- B: Nanunso inu, moyo ndi chonchotu. Nthawi ina iliyonse pamakhala opambana komanso olephera.
- C: umenewu ndiye moyo.
- B: tingonena kuti amene akufuna kupulumuka ku ngozi za kusintha kwa nyengo sakuyenera kugona tulo koma kuchilimika kuti apeze njira zodzithandizira yekha mosadalira boma kapena ena kwambiri.
- C: Aliyense ndithu akuyenera kutero.
- A: pakati pa nyama zakutchire
- D: komanso ine anthu.
- A: tikulankhula pano enanutu pano simungagone bwino ata chifukwa chotentha.
- D: Akakhala ana anu ndi nkhalamba zanu ndiye ali pa chiopsezo chachikulu ndi kusintha kwa nyengoku.
- C: tikuuzidwa kuti kukubweraku, madera ambiri adzakhala opanda anthu chifukwa chotentha kwambiri.

Next: B

- B: tikulankhula pano, anthu ambiri akuthawa kale ku mayiko awo chifukwa cha nkondo.
- C: Malo akuchepa padziko chifukwa cha anthu othawa nkondo. Nanga akadzapatikizana ndi othawa ngozi zadzidzidzi, zidzatha bwanji?

[Klick to Picture 46]

GAWO 8 [Picture 55 and Picture 56, change automatically from Picture 54!!!]

- B: Ndimakhala my Nyanja zikuluzukulu. Sindikonda kukhala ndekha koma mmagulu ndi anzanga ena. Kufunika kwanga simumakuona komatu ndine wa phindu.
- [Klick to Picture 56]**
- D: Inetu ndi anzanga sitingapilire kutentha kwa madzi mu Nyanja zathu.
- B: Ndikidziwa kuti enanu mukuyesetsa kutithandiza kuti ine ndi anzangatisafe. Komatu ngati madzi angapitilire kutentha kuposa mmene zilili pano, ifetu tifa ndithu.
- D: Ndithutu madzi aonongeka. Tikufa ife pamodzi nd zomera za mmadzi.
- B: Matayala akutha omwe muma taya mmadzi pamodzi ndi nyansi zina zikupha nsomba komanso zomera za mnyanja.
- D: Anthu mumaiwala chinthu chimodzi chofunika kwambiri. Zolengedwa zimadalirana. Choncho, chilichonse cholengedwa nchofunikatu.
- B: Kumbukirani kuti madzi osefukira, sivuto kwa kwa chilichonse cholengedwa. Mwachitsanzo chabe, nsomba zimasangalala zedi madzi akasefukira.
- D: Kwa inu anthu, madzi osefukira ndi vuto lalikulu komatu kwa ife ma coral reef timasangalala nako.
- B: Zitionongani komatu tsiku lina mudzatifuna. Mudzatilira. Osati chifukwa ndife owoneka bwino ayi koma chifukwa choti ndife amene timakusamalirani nsomba mmadzi a mnyanja.
- D: Ziyerekedwani pano komatu tsiku lake ndi limodzi, mudzatifuna.

Next: B

- B: Madzi akadzachuluka mu nyanja za mchere, nkuyamba kusefukira mudzawakumbuka mawu angawa ndithu.
- D: Komatu ife kudzakhala kulibeko nthawi imeneyo. **[Klick to Picture 57]**

GAWO 9 [Picture 66 and Picture 67, change automatically from Picture 65!!!]

- C: Inetu ndimakhala ku Amerika. Ndine mtengo waukulu kwambiri. Nthambi zanga zimakula kwambiri. Ndine wa dzina labwino komanso wa mphamvu. Ndiliba maganizo osowa pa dziko la pansi pano posachedwapa. Ubwino wake mudakandidzalabe ngakhale kwinku mukundidulanso.
- A: Mbuyomu anthu ankapanga ma bwato pogwiritsa ntchito matabwa ochokera ku mtengo wanga. Komanso ngakhale ma gitala ndi zina zotero zimapangidwa kuchokera ku matabwa anga. Nyengo zimasinthadi.
- C: Kalekale munkawenga mafuta pogwiritsa ntchito njira zabwino zosaononga chilengedwe. Panotu ngakhale mafuta omwe mukuwenga mafuta osakanikirana ndi madothi chifukwa cha njira zoipa zomwe mukugwiritsa ntchito masiku ano.
- A: Nchifukwa chake kuti mupeze 1 litre ya mafuta ku Canada, mumagwiritsa ntchito 5 litres ya madzi.
- C: Musaiwale kuti nchifukwa chake matenda ngati cancer ikukuvutani kwambiri masiku ano. Mukamapanga mafuta mumasunga zotsalira zake munyanja zanyansi. Nyansizi zimathera mmitinje ndi mmadzi a pansi pa nthaka. Choncho nkumati cancer ndi matenda ena nkuchepa?
- A: Ngakhale anthu omwe amagwira ntchito popanga mafuta amagwiritsidwa ntchito ngati akapolo.
- D: Kuchotsatu mafuta mu nthaka kumaononga chilengedwe kwambiri.

Next: B

GAWO 10 [Picture 80 and Picture 81, change automatically from Picture 79!!!]

- D: Tikhoza kulankhula mmalo mwa nyama zonse ndi zomera zomwe.
- C: Kuyambira kwa **Krill** mpaka ma **whales**.
- B: Ndi ma elks mpaka njovu.
- A: Nyama zamwayi zimene zidakali moyo.
- C: Paja zina munazidya kale.
- D: Tsiku limodzi silingakwane.
- A: Buku lopatulika, Baibulo, limakamba za chigumula cha Nowa chifukwa cha uchimo padziko lapansi.
- D: Koma simukutanthauzira molakwika ?
- B: Zimafotokozedwa bwino mu nthano
- C: Nkhani yachigumula imapezekanso mu nthano ya Epic of Atra Hasis mnzke zambuyomo. Mmeneno amati

Mawu ochokera kumbuyo:

“thawani mnyumba, konzani mabwato, tayani katundu kuti mupulumutse moyo wanu”.

- A: Za izi timadziwa. **[Klick to Picture 81]**
- C: Timadziwa kuyambira kalekale kuti zinthu nzofunika mmoyo wathu.
- D: Koma taiwala chinthu chimodzi chofunikira kwambiri.

Mawu ochokera kumbuyo:

“Siyani akatundu anu onsewo. Sankhani moyo. Tayani zonse za pansi pano kuti mupulumutse mzimu wanu ».

- A: Pajatu anthufe ndi akatswiri popondereza zolengedwa zina. **[Klick to Picture 82]**

GAWO 11 [Picture 87 and Picture 88, change automatically from Picture 86!!!]

- D: Ndimapezeka paliponse pa dziko lapansi pano. Dzina langa ndine munthu. **Next: B**
[Klick to Picture 88]

- B: Muchilankhulo cha latin, ndimatchedwa **homo sapiens**. Dzina langa limatanthauza kuti ndine “womvetsa, mlangizi, wanzeru, wochenjera komanso oganiza”.
- C: Ndikupangitsa kusintha kwa nyengo (climate change) ndi ine ndithu. Komanso choseketsa kwambiri ndi chakuti amene amavutikanso kwambiri ndi kusintha kwa nyengo ndi ine ndemwense.
- A: Amene akufuna mpweya wabwino, madzi a ukhondo, chakudya chabwino komanso ngakhale chitetezo ndi inenso.
- C: Munthu amachita chili chonse chothekera kuti apeze mtendere ndi moyo ofewa pa dziko pano.
- D: Komanso nthawi zina popanga izi, sasamala za zolengedwa zina.
- B: Nchifukwa chake munthu akuyenera kudzida yekha ngati zalakwika pa dziko lapansi pano.
- A: Mulungu akhoza kutumiza chigumula china ngati cha nthawi ya Nowa malinga ndi mmene anthu akuchimwira pansi pano.
- D: Ndi mmene anthu akuchimwira masiku ano, izi tiziyembekeza kuti zikhoza kuchitikanso nthawi ina ili yonse. Zikungoyenera kutero.
(onse owerenga nkhanayi adzuka ndi mapepala awo ngati nkhanayi yatha. Kenaka akhala pansi kuti amalize nkhanayi)
- B: Mvula bwera bwera. *3. Mmene ikugwera mvulamu timupemphe Mulungu kuti agwetse nzeru pakati pa anthu chimodzimodzi.
- C: Kuti anthu adziwe kuti tikhoza kuchitapo kanthu poteteza dzikoli ku ngozi za chilengedwe.
- A: Inetu si Nowa ayi koma sindikakonde kuti chionongeko chinansi chidzabwere pa dzikoli ngati mmene zinachitikira nthawi ya Nowa.
- D: Tamverani.
- A: Nkhani tikunena panoyi siyongocheza ayi.
- C: Tiyeni tiyambe kuchitapo kanthu pothetsa kusintha kwa nyengo.
- B: Sitikufuna kuti tsiku lina tidzanong’oneze bondo zinthu zitafika poti sizingakonzekenso ayi.

Next: A



- A: Mwandiona ine pamodzi ndi anzagawa? Takusonyezani kuti nzotheka kugwiritsa ntchito njira zabwino poyenda maulendo osawononga za chilengedwe. Mmalo mwa galimoto, njinga.
- B: Ngakhalenso sitima mmalo mwa ndege.
- C: Komanso osamagoyenda yenda ngai nkosafunikira kutero kukhala pakhome pa kwanu basi. Chifukwa maulendo ena ngofunikira komanso alipo ena opanda phindu.
- D: Zinthu zomwe tili nazo tizizigwiritsa ntchito nthawi yayitali.
- A: Zinthu zikaonongeka mmalo mozitaya tizikonza ndi kugwiritsanso ntchito.
- B: Mwandiona ine, sindiyatu nyama.
- C: Ine ndiye ndimadya koma mpang'ono kwambiri komanso patalipatali.
- D: Inenso sindidya nyama.
- A: Nzosakwanira kungopewa kudya nyama.
- D: Komabe ku mbali yanga ndikuyesetsa kuteteza chilengedwe pochita zimenezi.
- A: Nchifukwa chake tikukusonyezani kuti nzotheka aliyense kuchitapo kanthu mwa kuchepekedwa kwake.
- B: Tiyeni tigwire ntchilo limodzi anzanga tonse.
- C: Kaya ndi inu andale
- D: kaya ndi inu ogwira ntchito ku banki, kaya ndi ine a phunzitsi, ana a sukulu.
- A: Kutu tisinthe maganizidwe komanso machitidwe athu oipa amene akupangitsa kusintha kwa nyengo.
- B: Musadzidelere poti ndi inu ana a sukulu, pakuti muli ndi kuthekera.
- C: Ena li ndi mphamvu zochepa
- D: Ndatitu, ine si Nowa ayi.
- A: Komanso pano palibe Nowa.
- ALL:** Koma tonse ndife gawo limodzi la chombo cha Nowa. **[Klick to Picture 89]**



GAWO 12 [Picture 101, 102, 103, 104,....., change automatically from Picture 100!!!]

Zithunzi ndi ma vidiyo

Ine dzina langa ndi

Ndimachokera ku dziko la

Ndine mmodzi mwa anthu omwe akugwira ntchito yoteteza za chilengedwe kuti tithane ndi kusintha kwa nyengo.

Kenaka zokambirana zokhudza ndi kusintha kwa nyengo